Mulungu Anayankha Pemphero Lake

Malangizo: Chitani zotsatirazi muli pamalo opanda phokoso. Pamene mukuwerenga mavesiwa, yerekezani kuti mukuona zinthuzo zikuchitika. Mukhale ngati mukumva zimene anthuwo akulankhula ndiponso mmene akumvera mumtima mwawo.
Amene akutchulidwa kwambiri m'nkhaniyi: Nehemiya, Mfumu Aritasasita, Sanibalati ndi Tobiya
Chidule cha nkhaniyi: Nehemiya anapemphera kwa Mulungu, anapempha kwa mfumu kuti amulole kupita ku Yerusalemu, komanso anathana ndi zopinga zambiri.

1 GANIZIRANI ZIMENE ZINACHITIKA.—WERENGANI NEHEMIYA 2: 1-20.

Kodi mukuganiza kuti anthu amene atchulidwa m'nkhaniyi ankaoneka bwanji?

Nehemiya: _____

Mfumu Aritasasita: _____

Sanibalati ndi Tobiya: _____

Mukuganiza kuti n'chifukwa chiyani pemphero la Nehemiya linali lachidule? _____

_____

Kodi mukuganiza kuti mzinda wa Yerusalemu unkaoneka bwanji pa nthawi imene Nehemiya anafikako? (*Werenganinso vesi 13 ndi 14.*)

_____

Kodi mukuganiza kuti mawu a Nehemiya amene ali pavesi 17 ankamveka bwanji?

_____

2 FUFUZANI MOZAMA.

Kodi mukuganiza kuti Nehemiya anapempherera chiyani? (Werengani Nehemiya 1: 4-11.)

_____

N'chifukwa chiyani mukuganiza kuti Nehemiya ankakhulupirira kuti Aritasasita amulola kuti apite ku Yerusalemu? (Werengani Ezara 7:1-6; Miyambo 21:1.)

_____

Kodi Ayuda 'analimbitsa bwanji manja awo kuti agwire ntchito yabwino'? (Werengani Nehemiya 2:18; Yesaya 35:3.)

_____

www.jw.org © 2013 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

N’chiyani chikukuchititsani chidwi muganizira zimene Nehemiya anayankha Sanibalati ndi Tobiya? (Werengani Nehemiya 2:20.)

_____

3 GWIRITSANI NTCHITO ZIMENE MWAPHUNZIRA.

Lembani zimene mwaphunzira zokhudza . . .

Mphamvu ya pemphero. _____

_____

Mmene Yehova Mulungu amathandizira atumiki ake akamalankhula molimba mtima. _____

_____

4 DZIFUNSENI KUTI:

Kodi ndingatsanzire bwanji Nehemiya ndikakhumudwa kapena ndikakhala ndi nkhawa?

_____

_____

Anthu ena akamatsutsa zimene ndimakhulupirira, kodi ndingasonyeze bwanji kuti ndimakhulupirira Yehova?

_____

_____

M’nkhaniyi, kodi ndi mfundo iti imene yandikhudza mtima kwambiri, ndipo n’chifukwa chiyani?

_____

_____

_____

Mungachite izi: Pogwiritsa ntchito mapu, pezani pamene mzinda wakale wa Susani ndiponso wa Yerusalemu. (Nehemiya 1:1) Werengetserani mtunda wa pakati pa mizindayi m’makilomita ndipo ganizirani mmene inuyo, mofanana ndi Nehemiya, mukanavutikira kuyenda ulendo umenewo.

JW.ORG™

Koperani nkhaniyi pa www.jw.org

www.jw.org © 2013 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania